Kodi Zoona Zenizeni za Mulungu N’zotani? —Gawo 1

Nkhaniyi yachokera m’buku lakuti *Kodi Baibulo Limaphunzitsa Chiyani Kwenikweni?* mutu 1. Mungalipeze pa www.jw.org.

ZIMENE MUYENERA KUCHITA: Ganizirani mozama zimene mumakhulupirira ndiponso chifukwa chake mumazikhulupirira. Fufuzani zimene Baibulo limaphunzitsa kenako onani mmene mungafotokozere ena zimene mumakhulupirirazo.



KODI MULUNGU AMAKHUDZIDWA IFEYO TIKAMAVUTIKA?

1 GANIZIRANI MOZAMA ZIMENE MUMAKHULUPIRIRA

Kodi mukuganiza kuti ena angayankhe bwanji?

.....

.....

Kodi **inuyo** mumakhulupirira zotani?

.....

.....

N’chifukwa chiyani mumakhulupirira zimenezo?

.....

.....

www.jw.org © 2014 Watch Tower Bible and Tract Society of Pennsylvania

2 FUFUZANI ZIMENE BAIBULO LIMAPHUNZITSA

Si Mulungu amene amachititsa zinthu zoipa koma amangolola kuti zizichitika.

(Werengani mutu 1 m'buku lakùti *Baibulo Limaphunzitsa Chiyani* ndime 6 mpaka 8.)

Werengani Yakobo 1:13.

Kodi lembali likusonyeza bwanji kuti si Mulungu amene amachititsa mavuto?

.....

.....

.....

Kodi mungapereke chitsanzo chotani chosonyeza kusiyana pakati pa **kulola** zinthu kuchitika ndi **kuzichititsa?**

.....

.....

.....

Mofanana ndi bambo amene ali ndi mwana wosamvera ndipo mwanayo wasankha kuchoka pakhomo, Yehovanso amalola anthu kusankha zimene akufuna kuchita. Koma si Yehova amene *amachititsa* mavuto amene anthuwo amakumana nawo chifukwa cha kusamumvera kwawo.

www.jw.org © 2014 Watch Tower Bible and Tract Society of Pennsylvania

Mulungu amatikonda ndipo sasangalala tikamavutika.

(Werengani mutu 1 m'buku lakuti *Baibulo Limaphunzitsa Chiyani* ndime 11 mpaka 13.)

Werengani Genesis 6:5, 6.

Kale, Yehova "zinam'pweteka kwambiri mumtima" pamene zinthu zoipa zinachuluka padzikoli. Kodi tikudziwa bwanji kuti amamvanso chimodzimodzi masiku ano? **(ZOKUTHANDIZANI:** Werengani Malaki 3:6.)

.....

.....

.....

Werengani 1 Petulo 5:7.

Kodi mukuganiza kuti n'chifukwa chiyani Yehova amatiuza kuti tizimuuza mavuto athu m'pemphero?

.....

.....

.....

Werengani Genesis 1:26 ndi 1 Yohane 4:8.

Popeza **ifeyo** sitisangalala tikamaona anthu akuvutika, n'chiyani chingatithandize kutsimikizira kuti nayenso **Yehova** zimamukhudza?

.....

.....

.....

Kodi inuyo mumamva bwanji mumtima mwanu chifukwa chodziwa kuti Mulungu sachititsa mavuto, amatikonda ndiponso sasangalala tikamavutika?

.....

.....

.....

www.jw.org © 2014 Watch Tower Bible and Tract Society of Pennsylvania

3 FOTOKOZANI ZIMENE MUMAKHULUPIRIRA

NGATI WINA WANENA KUTI…

Mulungu amalanga anthu oipa powabweretsera mavuto.

MUNGAYANKHE KUTI…

Zipembedzo zambiri zimaphunzitsa choncho. Koma ine ndimakhulupirira zosiyana ndi zimenezo chifukwa . . .

.....

.....

Kodi mungawerenge lemba liti kuti mumuthandize?

.....

N’chifukwa chiyani mumakonda lemba limenelo?

.....

NGATI WINA WANENA KUTI…

Mulungu ndi wamphamvu yonse. Zikanakhala kuti iye amatikondadi, sakanalola kuti tizikumana ndi zinthu zoipa.

MUNGAYANKHE KUTI…

Ndikugwirizana nazo zoti Mulungu ndi wamphamvu yonse. Koma sindikukayikira kuti *amatikonda* chifukwa chakuti. . .

.....

.....

Kodi mungawerenge lemba liti kuti mumuthandize?

.....

N’chifukwa chiyani mumakonda lemba limenelo?

.....

www.jw.org © 2014 Watch Tower Bible and Tract Society of Pennsylvania